CHIFUKWA CHIANI CHENJEZOLI?

M'matauni a ku Malawi kuno, ngakhalenso ku Ulaya, Amerika, ndi ku Joni, timakumana ndi atsikana ndi amai ambiri okhumudwitsidwa ochokera ku Malawi.

Amenewa amakhala atanamizidwa:-

- ntchito yapamwamba
- ya malipiro abwino
- ukwati wosangalatsa
- ndi zina zambiri zoterozo

Tsono iwowo amakhulupirira kuti akalemera patapita nthawi yochepa.

Koma kawiriwiri zoona kwenikweni ndi ziti?

1. Kuli ulova wa ndiweyani, tsono ndi kwapatali kwa inu kupeza ntchito.

2. Mukapita dziko lakutali mudzasowa chilolezo chogwirira ntchito ndi chokhalira ku dzikolo. Popanda zimenezi mudzagwidwa ndi kutumizidwa kwanu.

3. Kulikonse kuno ku Malawi kapena kunja mahule amafunika kwambiri. Basopo! Mwina akufuna inuyo!

4. Chenjerani! Mapangano abwino ambiri sioona ndipo satsatidwa.

Ngati mukufunitsitsabe kupita kunja...

1. Onetsetsani kuti mukudziwa maina ndi ma adresi a anthu amene akukutenganiwo. Funsafunsani ngati pokutenganipo sakuphwanya malamulo ena aliwonse.

2. Kayankhuleni ndi kazembe wa dziko Lomwe mukupitalo. Funsani ngati amene akukulembani ntchitoyo alipodi ndipo ngati ali munthu wokhulupirika.

3. Tsiku lonyamuka dziwitsani banja lanu ndi abwenzi anu za adresi ya kumene mukupita, maina a gulu kapena anthu amene mudzayende nawo ndipo apatseni chithunzi chanu chojambulitso posachedwa.

Anthu sali pa malonda

4. Yesetsani kudziwa mabungwe othandiza alendo a ku maiko ena – mungathe kufunsa ku CFSC, kapena mabungwe ena a ku Malawi kuno ndikuwafunsa zofuna zanu – amene angathe kukuthandizani kunja kwa dziko mutakumana ndi mavuto.

Ngati mwalembedwa ntchito m'boma lina m'Malawi momwe muno

1. Yesetsani kudziwitsa a banja lanu, abwenzi, achibale za kumene mukupita kukakhala ndi mtundu wa ntchito imene mwalembedwa.

2. Musakongole ndalama zambiri pokhulupirira kuti mudzalipira ngongole yanu ndi ndalama za ku ntchito kwanuko.

3. Nthawi zonse muli ndi ufulu wanu wachibadwidwe kukanira okulembani ntchito kapena a m'banja lanu kukagwira ntchito yokuchotsani ulemu (mwachitsanzo, kutumikira m'nyumba yomwera mowa).

4. Musamakhulupirire nkhani zonse za ntchito za malipiro ambiri kuti zikudikira inu m'matauni monga Lilongwe kapena Blantyre – dziwani kuti ku dziko kuno kulinso anthu ambirimbiri amphawi amene akufunafuna ntchito.

5. Yesetsani kuti musapezeke ku malo akutali ndi banja lanu kapena anansi anu. Ngati muli nawo kutali, pemphani wina kuti adziwe ku malo kumene muli.